## TIYENI TITENGE UMWINI KOMASO GAWO POSAMALI RA NDIKUTETEZA ZIPANGIZO ZA MAGETSI A MAREP

1. Musalore kuti wina aliyense awononge kapena kuba zipangizo za magetsi a MAREP monga, nthambo, ma wire, copper ndi zina.
2. Khalani tcheru ndipo pamene wina waba kamunenezeni ku police yomwe muli nayo kafupi.
3. Dziwani kuti, magetsi a MAREP ndi anu, boma linapeleka magetsiwa kwa inu, choncho tengani umwini, poteteza ndikusamala zipangizo za magetsizi.

## DZIWANI ZA NDONDOMEKO YA NDAWALA

1. NDAWALA ndi ndondomeko ya boma yomwe ili pansi pa Pologalamu ya MAREP.
2. Cholinga cha ndondomekoyi ndikuthandiza anthu a madela komwe magetsi a MAREP anafika kale koma alibe kuthekera koitanitsa magetsi komaso kupanga nyumba zawo wiring.
3. Anthu ochepekedwawa amathandizidwa polumikizilidwa magesi pa ngongole yomwe imabwezedwamwapang'onopang'ono munthu akamagula magetsi.
4. Ndondomeko ya NDAWALA sifikira aliyense , Dela lililonse limapatsiwa nambala ya anthu omwe atapindule nawo mu ndondomekoyi ndipo opindula mu ndondomekoyi amakhala okhaokha omwe alibe kuthekera kopeza ndalama zoitanitsira magetsiwa pawokha.

Printed by: Mega Pixels Ltd 0993273390

CONTACTS US
**The Director of Energy**
Capital House, Second Floor
Private Bag 309, Lilongwe

**Tel:** +265 1 789 385
**Email:** info@energy.gov.mw
**Website:** energy.gov.mw

UNITY AND FREEDOM

Ministry of Energy

# MALAWI RURAL ELECTRIFICATION PROGRAMME (MAREP)





## MAREP NDI CHIYANI

1. MAREP imaimila Malawi Rural Electrification Program
2. Imeneyi ndi pologalamu ya Boma imene ikuyendetsedwa ndi Unduna wa zamagetsi
3. MAREP ndi ndondomeko ya boma, yoika magesti m'madela akumudzi komaso ma trading omwe bungwe la ESCOM silingafikire.
4. Madela omwe kumapita magesi amasankhidwa mogwilizana ndi ma komiti a District Council momwe atsogoleri onse am'midzi amakhalamo ndi oyimilililidwa wawo.
5. Cholinga cha MAREP ndikuchulukitsa chiwerengero cha anthu ogwilitsa ntchito Magetsi m'madela aku midzi pofuna kuthetsa umphawi komanso kupititsa pasogolo ntchito zachuma.
6. Pologalamuyi, imachitika muzigawo zigawo, ndipo chigawo chilichonse chimakhala ndi chiwerengero cha madela omwe atafikilidwe.
7. Pakali pano chigawo cha MAREP 8 chilikumalecheleche ndipo zokonzekera za gawo la 9 zinayambika kale.













## TITANI POMWE MAGETSI A MAREEP AFIKA MDELA LATHU?

1. Pangitsani olo ikitsani mawaya a magetsi nyumba yanu, zomwe pachizungu amati wiring.
2. Katengeni ndi kufila ma form oyitanitsira magetsi ku office ya ESCOM.
3. Mukatero lipirani ndalama yomwe yakhazikitsidwa pa nthawi imeneyo.
4. Ogwira ntchito ku ESCOM adzakuyenderani kuti aone ngati wiring yanu inapangidwa molingana ndi ndondomeko zovomelezeka.
5. Dikirani kutia ESCOM wo adzakuyikireni chingwe cha magetsi kuti muyambe kukhala mowala.

Dziwani kuti pamene mwalipira ku ESCOM!!! Simukuyenera kupeleka ndalama iliyonse kwa munthu kapena ogwira ntchito ku ESCOM.

## ZOPINDULITSA ZOBWELA NDI MAGETSI A MAREP

1. Kupititsa pasogolo maphunzilo popeza ana amatha kuphinzila olo kuwelenga usiku.
2. Zokudya zimasungika poikidwa mmalo ozizila (fridge)
3. Ntchito za lamya zimapita patsogo ndipo anthu amatha kulumikizana ndi anzawo kudzela pa lamya komanso makina a intaneti.
4. Magesti amapitisa patsogolo chitetezo powunika bwino mmisewu ya anthu oyenda pansi komanso pounika bwino zikwangani za chenjezo mmisewu ya galimoto.
5. Amapititsanso patsogolo ntchito za chipatala m'midzi popangisa kukhala kothekela kugwilitsa ntchito zipangizo zamagetsi komanso kusunga mankhwala ena amene amafunika malo ozizira.